UTHAWE NDI KAMAPHA
ife toto
KACHIROMBO KA KORONA

ELS VAN HEMERT

Wojambula
Mieke Linssen

AISHA & friends

Dutch Tanzania Foundation

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Uthawe ndi Kamapha akusewera panja.

Kwenikweni adakayenera kukhala ali ku sukulu tsopano koma masukulu adatsekedwa. Aphunzitsi adawawuza za nthenda yina yomwe yikusautsa mtundu wa anthu pa dziko lonse lapansi. Aphunzitsi adafotokoza momveka kuti ndi chifukwa chake ana sakupita'nso ku sukulu. Poyamba, kudali kwapatali kumvetsetsa koma poti Uthawe ankamvetsera bwino ndithu,adaona monga kudali kofunika kukhala ku nyumba nthawi yino.

Koma Kamapha sankamvetsetsa chifukwa maganizo ake adali kwina pamene aphunzitsi ankafotokoza za kachirombo kaja. Uyu ngwopupuluma; maganizo ake ndi wongofuna kusewera mpira ndi anzake panja.

Koma poti lero ali ndi Uthawe, akufuna kudziwa za nthenda imene ili pakamwa pa ali yense. Kamapha anayamba kudabwa ndi m'mene ali yense akukhalira koma'nso nkhani yosawonana ndi kuchezana ndi anzake ku sukulu. Tamuwonani, watenga mpira uja ndi kukhala pansi.

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Akuti “Iwe Uthawe, kodi ungandiuze’nso zimene aphunzitsi adanena za kachirombo kaja?”

Uthawe adavomera, nakhala pansi, nati: “Dzina la kachirombo’ka akuti ndi **kachirombo ka korona**. Kachirombo’ka ndi kakang’ono-ng’ono kosawoneka ndi maso, ayi, ndipo ndi kowopsa kwambiri”. Kamapha anamudula mawu, nati:” Ukuti nkowopsa kwambiri, koma nkowopsa kwambiri bwanji ngati sikaoneka?”

Uthawe adati: “Vuto ndi limene’lo poti sitikaona,sikuti palibe ayi koma kangathe kukhala pali ponse. Kachirombo ka korona, adokotala amangokatchula kuti “kovidi-19,” chidule chimenecho. Ndi nthenda yowopsa yomwe ungadwale nayo kwambiri. Umamva ngati chimfine, malungo,chifuwa,mutu, koma chifuwa chake chimakhala chopweteka kwambiri,mwina mpaka kubanika nacho.



© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Kamapha adakhala duuu…. Kuganiza…, kenaka waliponya funso: "Koma'be sindikumvetsa chifukwa chiyani tidaleka kupita ku sukulu?"

Uthawe adati, "kachirombo'ka nkopatsirana, ndiye kuti nkopatsirana mosavuta". Tiyese kuti uli ndi matope m'manja mwako'mu, nukhudza ku maso kwako'ku,kapena kutola mpira,kaya kukhudza mnzako…, kodi wawona m'mene matope aja angamatire apa ndi apo?" Kamapha adadzidzimuka, nati: "Tsopano ndawona!"

"Tsono nkhani ya kachirombo ka korona ndi yomwe'yi. Ukatsokomola,ukayetsemula,ukakhudza wina kapena kupatsana naye moni wa pa dzanja, basi, ndi mwachidule kupatsira kachirombo'ka mnzako'yo. Kachirombo'ka kangathe kukhala ponse-ponse n'kumangofarikira, iwe'yo wosadziwa."

Kamapha adayankha, nati, "Kalanga ine!.Matope ungawawone ngati wa khudza mnzako, ichi ndi chomveka."

"Ee,zoona'di, kusiyana kwake ndi kwakuti matope ungawawone koma kachirombo kaja, ayi. Apa ndiye pagona nkhani: kukhala ndi kachirombo'ka sikuti pompo ukudwala, ayi.Ungathe kumayenda nako, iwe'yo wosadwala; kumva chifuwa kapena malungo, ayi, koma uli mkati mokafaritsa, pamene ena'wa ali mkati mopatsirana ngati mnzere. Ena mwa iwo'wo' angathe kumadwala, ena nkumangofaritsa ponse-ponse. Ndiye kuti kachirombo'ka ndi mliri weni-weni."

Kamapha nkhawa ili biii, adati: "Poti sitingakaone…, tsono kali kuti…?"

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

“Kachirombo’ka kali ponse-ponse: ku msika kumene ali yense amapita kugula mbatata yakholowa, anyezi,tomato,kaya masamba. Kangakhale’nso mu bus,mu tchalitchi, mu mzikiti ndipo’nso mu sukulu. Ku malo onse’wa, anthu amakhala mothinana,tsono nchapafupi kupatsirana kachirombo’ka. Nchifukwa chake tidaleka kupita ku sukulu ndi ku tchalitchi komwe; timangopemphera ku nyumba.”

“Tsono titani nanga?”

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Malamulo alipo oletsa kufalika kwa kachirombo'ka.

Poyamba muzisamba bwino m'manja mwanu ndi sopo,nthawi yokwanira 20 sekondi. Koma'nso muzitero kawiri-kawiri.

MUSAMBE BWANJI M'MANJA MWANU'MO?

Musambe ndi madzi.

Musambire sopo ngati alipo.

Mukhale mukusamba m'manja'mo kwa 20 sekondi; kufikisa ndi kupisitsa zala pakati pa zinzake, osaiwala kukolowola mu zikhatho.

Mutsukuluze bwino m'manja'mo.

Mukutumule madzi a m'manja mwanu'mo.

Mupukute m'manja'mo ndi chopukutira cha ukhondo kapena kungodikira kuti muwume mokha.

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Muziika chigongono chanu pakamwa pamene mukufuna kutsokomola kapena kuyetsemula.

Musakhudze pakamwa, mfuno kapena maso.



Mukapita kumene anthu akukomana, musayandikirane; muzikhala patali-patali ngati mpata wa 1 mita ndi theka lake (1.5 meters) kuti kachirombo'ka kasakufikireni.

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Musayandikire munthu amene akumva chifuwa.



Muvale chodziteteza pakamwa pamene mukuyenda pa msewu kapena pa njira.

Musayende–yende ayi; khalani ku nyumba kupatula ngati simungachitire mwina. Ndiye kuti kukhala ku nyumba osakasewera ndi anzanu.

Musapatsane moni wa pa dzanja kapena kupsopsonana. Mudzingopatsana moni wa pakamwa ndipo muli wotalikirana.

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

“Ndipo iwe Kamapha, ukudziwa… anthu okalamba kapena odwala-dwala, ndi amene angadwale msanga ndi kachirombo’ka. Tsono ndi chofunika kudziteteza ndi kutetezana. Ena akuthandiza anzawo powagulira sopo kuti asunge ukhondo. Ena akugulira anzawo zakudya zosungidwa bwino m’mapukusi. Ena akutero mu njira ya mapemphero.

Mukadwala mukawonane ndi adokotala ku chipatala. Kumene’ko akakuyezani bwino ndi kukusamalani bwino monga m’mene angathere. Iwo’wo amavala zodziteteza bwino ku kachirombo kaja poti nawo’nso ali pa chiwopsezo. Iwo’wo atadwala, angasamale anthu odwala ndani? Nchifukwa chake ayenera kuvala zodzitetezera.”

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

“Aha!” Kamapha amangomvetsera nthawi yonse’yi zomwe Uthawe amanena. Koma mutu wake sukugwira, ayi. Akuganiza kuti Uthawe ndi wochenjera kudziwa zonse’zi.

Koma’be Kamapha akufuna kukasewera’nso; watopa nkukhala pansi, wayimilira, nkugwira dzanja la Uthawe kuti avine koma Uthawe akumuwuza kuti: “Iwe Kamapha,usandigwire dzanja kuti tivine. Si chanzeru kutero. Titalikirane 1 mita ndi theka. Lamulo likutero…. Tipeze masewera ena tsopano. Koma ndikuyesa kuti ndi bwino koposa kupita ku nyumba; tikasewere komwe’ko,iwe kwanu,ine kwathu.

Koma ngati ukundisowa’di,
ubwereke foni komwe’ko,
tsono tingathe
kucheza pa foni’po.”

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

“Uthawe, tsopano ndamvetsa bwino zonse, wandifotokozera bwino ndithu, zikomo. Ngakhale sindikuzikonda,koma ngati tonse titsata malamulo’wa, ndithu tingathe kugonjetsa kachirombo ka korona. Tikatero tidzayamba’nso sukulu; tidzatha kusewera, kuvina ndi kupsopsonana.

Pang’ono-pang’ono, moyo udzakhala’nso monga kale.

© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS

Based on an idea by Monique Kerpen.

COLOPHON:

This is a co-production by Dutch Tanzania Foundation and Aisha & Friends.

Author:	Els van Hemert | Jan & Ko | creative in education
Illustrated by:	Mieke Linssen | Jan & Ko | creative in education www.janenko.nl
Production support:	Monique Derrez | Dutch Tanzania Foundation www.dutchtanzaniafoundation.org Alberdine van de Hulsbeek & Mieke Linssen | Aisha & Friends www.aishaandfriends.com
Design and layout:	Anke van Horne
Translation in English:	Yo van Knippenberg | Femke Janssen
Translation in Swahili:	Walter Mgina
Translation in Chichewa (Malawi):	Sister Josefa Ng'ona
Translation in Chishona (Zimbabwe):	John Mutumburanzou
Also made possible by:	Fonds van Cultuurparticipatie Provincie Limburg Locaal C
With thanks to :	Nazareth Foundation Malawi (Ineke Hendrickx) IMBA International
Date:	May 2020

This book is also available in Cishona, Swahili, English and Dutch.



© THIS IS A CO-PRODUCTION BY DUTCH TANZANIA FOUNDATION AND AISHA & FRIENDS